



Tony Alamo kubatiza anthu amene angotembenuka mitima kumene ku Pacific Ocean kuyambira m'mawa mpaka usiku kwambiri

NDIKOSAVUTA KUNENA NTHAWI YA KUBWERANSO KWA AMBUYE PA DZIKO LAPANSI

Yolembedwa ndi Tony Alamo

MULUNGU watipatsa njira yosavuta yodziwira za m'bado wa kubweranso kwachiwiri kwa AMBUYE WATHU YESU KHRISTU. Ndithudi, MAWU a MULUNGU amatiuza kuti palibe munthu amene akudziwa za tsiku kapena ola lenileni. Komabe Yesu anatiuza za zochitika zosiyanasiyana zomwe zidzachitike mu m'badowo pamene kutha kwa dziko lapansi kudzakwanilitsidwe. Aliyense pa dziko lapansi panopa angathe kuona za kubweranso posachedwa kachiwiri kwa YESU KHRISTU pa dziko lapansi! (Mateyu chaputala 24).

AMBUYE sadzatisiya opanda kudziwa za nthawi yoyandikira kubweranso KWAKE kuposa mmene IYE akadalolera chiwerengero cha dziko lapansi cha mbali ina ya chigumula kusadziwa za nthawi yoyandikira chigumula choopsa.

Genesis 6:5-13 amati, "Ndipo MULUNGU anaona kuti kuipa kwa munthu kunali kwakukulu pa dziko lapansi [monga mmene ziliri lero], ndipo kuti malingaliro onse a mumtima mwake anali oipa okhaokha kosalekeza. [Kusakhanzikika kumeneku, (monga mmene zikuonekera) kulakalaka, kulota zoipa, zikuchitikanso lero, zaonjeze-

kera ndi mamiliyoni, chifukwa cha makina a magetsi (devices) komanso mgwirizano wa maunyinjii.] Ndipo zinamudandaulitsa MULUNGU kuti IYE analenga munthu padziko lapansi, ndi kumumvetsa chisoni IYE mu mtimwa MWAKE. Ndipo MULUNGU anati, ndidzamuononga munthu amene ndinamulenga padziko lapansi; onse munthu, ndi chirombo, ndi chinthu chokwawa, ndi mbalame zamlangalanga; chifukwa zimandidandaulitsa INE kuti ndinazilenga izo. Koma Nowa anapeza chisomo [mphamvu] m'maso a AMBUYE.

"... Nowa [ngati Yobu] anali munthu chabe komanso munthu wabwino kwambiri mu m'bado wake, ndipo Nowa anayenda ndi MULUNGU... Dziko lapansi linalinso loonongeka pamaso pa MULUNGU, ndipo linadzadza ndi ziwawa. [Ichi ndi china mwa zizindikiro! Ziwawa lero ndizoipitsitsa kwambiri chifukwa cha tekinoloje yamakono! China ili ndi zida zochulukika za nyukiliya zomwe zingaononge dziko lapansi chimodzimodzi Russia, North Korea, ndi maiko ena] Ndipo MULUNGU anaona dziko lapansi, ndipo, taonani, linali losokonekera; [mukukhulupilira kuti MU-

LUNGU akutionadi ife lero? IYE ndithudi akutiona!]¹ pakuti anthu onse anaononga njira zawo padziko lapansi. Ndipo MULUNGU anati kwa Nowa, Mathero a anthu onse adza pamaso pa INE; chifukwa dziko lapansi ladzadza ndi nkhanza kudzera mwa iwo; ndipo, taonani, ndidzawaononga pamodzi ndi dziko lapansi."

MULUNGU anauza Nowa kuti aseme chombo, kenako anampatsa malangizo a mmene angachisemere chombocho.² (Wina aliyense amene angadzapulumutsidwe mu chigumula chachikulu amayenera kukhala mu chombo, chimodzimodzi aliyense adzakhale Kumwamba ayenera kukhala mwa YESU. Chombo chinali ngati YESU. Tiyenera mwa UZIMU, kukhala mwa IYE, ndipo IYE, mwa UZIMU akhale mwa ife [Yohane 15:4-7, 17:20-23]!) Nowa analalika zoti kudzakhala kutha kwa thupi chombo chikadzatha, koma anthu anamuseka ndi kumulankhulira mawu a chipongwe, ngakhale ankaona kumalizika kwa chombo, chizindikiro cha nthawi! MULUNGU anasiya anthu kuti adziwe za kubweranso kudzera mwa ulaliki wa

(Yapitirira patsamba 2)

1 1 Sam. 2:3, 16:7, 1 Mbi. 28:9, 2 Mbi. 16:9, Mas. 33:13-15, 90:8, 94:7-11, 139:2-12, Miy. 5:21, Yes. 29:13-16, 66:18, Yer. 17:10, 23:23-24, 32:19, Dan. 2:20, 22, Zak. 4:10, Mat. 10:29-30, Mac. 15:18, Ahe. 4:13, Chiv. 1:8, 2:23, 5:6, 22:12-13 2 Gen. 6:14-16

NDIKOSAVUTA KUNENA NTHAWI YA KUBWERANSO KWA AMBUYE PA DZIKO LAPANSI

(Yachokera patsamba 1)

Nowa ndi pakupitiriza kumanga chombo! Iwo sanamvere, ndipo onse anaonongeka (Genesis 7:21-23).³ Onse a iwo!

Genesis 6:3, MULUNGU ananeneratu kuti zidzakhala zaka zingati IYE asanononge thupi ndi dziko lomwe. Dziko lapansi linali lokongola chigumula chisanachitike. “Ndipo AMBUYE anati MZIMU WANGA sudzakangana ndi munthu nthawi zonse, chifukwa iyenso ndi thupi la nyama: koma masiku ake adzakhala zaka zana limodzi ndi makumi awiri (120).” Tikutha kuona kuti AMBUYE anapereka kwa aliyense nthawi imene zizindikiro zambiri zoti athe kuona nthawi ya mathero awo kuti yatsala pang’ono. Ngakhale tisakudziwa nthawi ndi nyengo yeniyeni, tikuudziwa m’bado, omwe uli m’bado wa lero! (Mateyu 24:34-36).

Panali zizindikiro zoposa 300 zakubwera mwa thupi mwa AMBUYE ndi MPULUMUTSI wathu kuti tidzathe kudziwa nthawi yomwe MESIYA, EMANUELO, MULUNGU alinafe, adzatulukire.⁴ Panalibe kulakwitsa kuti IYE anali ndani,

ndi ndani, ndi kuti IYE akubweranso posachedwa kachiwiri.

Kubwera kwa YESU koyambilira kunali kosavuta kulosera, chimodzimodzi kubwera KWAKE kwachiwiri ndi kosavuta kulosera. Anzeru akummawa ndi abusa amene anabwera kudzamuona YESU atabadwa sanangodziwa za zizindikiro za nthawi zokha, komanso anatha kudziwa za zizindikiro za nthawi yomwe IYE adzafike (Mateyu 2:1-11).

“Atumiki [a YESU] anabwera kwa IYE payekha nati tiuzeni, kodi zizindikiro zimenezi zidzachitika liti? Nanga kodi chizindikiro cha kubwera KWANU chidzakhala chotani ndi chakutha kwa dziko? Ndipo YESU anayankha nati kwa iwo, yang’anirani kuti munthu asakupusitseni” (Mateyu 24:3-4). Ili ndi chenjezo lofunikira kwambiri! Kapena kuti, khalani atcheru lero ndi boma la dziko, ofalitsa nkhani, ndi matchalitchi abodza komanso mabiliyoni a anthu amene apusitsidwa ndi iwo. Osawamvera. Mwina mukuyembekezera kuona aneneri onyenga akutuluka m’matchalitchi? Ayi, ayi, si iwo okha. “Onetsetsani kuti PALIBE MUNTHU okupusitsani.” Zoona, ambiri amati iwo ndi KHRISTU, ndipo ambiri amati akuyankhulidwa ndi KHRISTU.

“Pakuti ambiri adzabwera mudzina LANGA, nkumati, ine ndine KHRISTU; ndipo adzapusitsa anthu ambiri. Ndipo mudzamva za nkondo komanso mphek-esera za nkondo [YESU akuti]: onani kuti palibe okusokonezani: chifukwa zinthu zonsezi zidzachitikadi, koma mathero ake sanafike. [Pano pali chizindikiro chimodzi:] pakuti mitundu idzaukirana, mafumu adzaukirana; ndipo kudzagwa zilala [ichi ndi chizindikiro chimene chikuchitika], ndipo miliri [imene imadza m’njira za matenda; amene alipo ambirimбири], ndi zivomerezi, mmalo osiyanasiyana. Zonsezi ndi chiyambi cha ululu wa mu mtima. Kenako adzakumasulani [kudzera mnjira za zinyengo] inu [ophunzira ANGA] kuti muzunzike, ndipo adzakuphani: ndipo mudzadedwa ndi mitundu yonse chifukwa cha DZINA LANGA [chifukwa timatumikira IYE]. Ndipo kenako ambiri adzalakwiridwa, ndipo adzaperekana wina ndi mzake, komanso adzadana. “Izi zandichitikirapo kambirimбири moti sindingawerenge kuti ndikangati.” Ndipo aneneri onyenga ambiri [wonama ndi iwo aumbo ni wabodza, pamodzi ndi mboni zabodza komanso oukira YESU] adzauka ndipo adzapusitsa ambiri [kudzera mukugwiritsa

3 1 Pet. 3:20, 2 Pet. 2:5 4 Tifunseni za buku laulele, *The Messiah According to Bible Prophecy*.

Makalata opita kwa Pastor Alamo

India

Okondeka abale ndi alongo a chifundo mwa Ambuye Yesu Khristu a Tony Alamo Ministries,

Moni kwa World Evangelist ndi M’busa wathu Reverend Tony Alamo pamodzi ndi mamembala otumikira amaudindo onse muutumiki wodalitsika komanso oyera mitima makamaka ku USA. Chikondi ndi mafuno abwino kwa inu nonse.

Tagwiritsa ntchito ndalama kugulira zinthu za anthu okhudzidwa ndi ngozi ya moto zomwe munatumiza kuti athandizikire. Anthu omwe anakhudzidwa ndi ngozi komanso anthu ena onse kuno akutamanda Ambuye m’ malo mwa inu chifukwa cha thandizo ndi chikondi choposa.

Tawapatsa zakudya, ziwiya zophikira, zovala zatsopano ndi ma Telugu Holy Bible dzulo monga pa 1-12-2012. Tathan-dizika kwambiri chifukwa cha thandizo lanu lofunikira.

Ine ndikukuthokozani nonse chifukwa chowathandiza anthu achisoni amene anakhudzidwa ndi ngozi. Mwa chikondi komanso mapemphero.

Taika zithunzi za ntchito za wachifundo zimene zinagwiridwa mmalo mwanu kwa anthu amene anakhudzidwa ndi ngozi kuno ku dera lathu. Tikufuna ma handredi a nkhani za m’makalata za Telugu za chitsitsimutso zothandizira ntchito za Uthenga Wabwino wa Ambuye. Tikufuna chisamaliro chanu chonse cha wachitsitsimutso ovutika ngati ine mu utumiki wa Ambuye pobweretsa miyoyo yomwe inasochera kupita ku chisamaliro cha chikondi cha Yesu Khristu kwa Mulungu Atate wa Kumwamba.

Tili ndi chikhulupiliro kuti timva kuchokera kwa inu. Ulemu kwa inu nonse chifukwa cha chikondi chanu komanso kukhudzidwa koposa. Onse akukupemphelerani



Kugawa zolembedwa pa sitolo yogulitsira zovala pamalo a malonda ndi M’busa Chinta

umoyo wabwino ndi kupita patsogolo komanso kwa okonedwa wathu woyera mtima Tony Alamo. Chonde onani mafailo omwe taphatikiza ku kalatayi. Mtumiki mzanu wodzichepetsa ndi wa chikondi mwa Yesu Khristu, V.R. Raju Chinta, M’busa Tony Alamo Christian Ministries Jayanthi Colony, Ambajipeta, E. G. District, A. P., India

ntchito ofalitsa nkhani mdziko la boma limodzi, ndi matchalitchi, motsogozedwa mwachinyengo ndi Vatican yaku Rome]. Ndipo chifukwa tchimo lidzacheluka, chikondi cha ambiri chidzazilala [ambiri adzasiya kutsatira AMBUYE]. Koma iye wakulimba kufikila kuchimaliziro, yemweyo adzapulumuka” (Mateyu 24:5-13). AMBUYE, kodi izi zikutanthauza kuti ngati sitilimba mpaka ku chimaliziro, ndiye kuti sitidzapulumutsidwa?⁵ Inde! ndizomwe IYE ananena, ndipo ndizosatheka IYE kunama (Ahebri 6:18).

Uwu ndi ulosi weniweni wochitika: “Ndipo uthenga wabwino wachifumu umenewu udzalalikiwa padziko lonse mwa umboni ku mitundu yonse ; ndipo kenako chimalizilo chidzafika. [Izi zikutanthauza kuti ziphunzitsa zonama, zilungamo za theka zambirimbiri kapena zopembeza mafano, monga zikhululupilo za a Katolika ndi ziphunzitsa zina zabodza; zikuthanthauza UTHENGA wa BWINO WACHILUNGAMO!] Kotero ngati mungaone chonyasa cha ku pululutsa, chimene chidanedwa ndi Mneneri Danieli, chitaima mmalo woyera [khalani mwa YESU MAWU, MZIMU]” (Mateyu 24:14-15). “Chonyasa cha kupululutsa” lero ndi boma

la dziko limodzi, tchalichi cha bodza komanso chofalitsa nkhani—zonse za satana.⁶

“Pakuti pomwepo kudzakhala masautso akulu, monga sadakhalepo otero kuyambira chiyambi cha dziko kufikila tsopano, ayi, ndipo sadzakhapono. Ndipo adaleka kufupikitsa masiku awo, sakadapulumuka munthu aliyense : koma chifukwa cha osankhidwawo masiku awo adzafupikitsidwa” (Mateyu 24:21-22).

“Tsopano phunzirani za fanizo la mtengo wa mkuy u ; Pamene tsopano nthambi zake zili za nthete, niphukila masamba ake, muzindikire kuti dzinja yayandikira: chomwechonso inu, pamene mudzaone zimenezo, zindikilani kuti wayandikira, inde pamakomo. Indetu ndinena kwa inu, M’bado uwu sudzatha kuchoka kufikira zinthu zonzezi zitachitidwa” (Mateyu 24:32-34).

“Ndipo monga masiku a Nowa, kotero kudzakhala kufika kwa MWANA wa MUNTHU. Pakuti monga mmasiku aja chigumula chisanafike anthu anali kudya ndi kumwa, anali kukwatira ndi kukwatiwa, kufikira tsiku lomwe Nowa analowa muchingalawa, Ndipo sanadziwa kanthu kufikira pamene chigumula chinadza, chinapululutsa iwo onse; kotero kudzakhala kufika kwake kwa MWANA wa MUNTHU” (Mat-

eyu 24:37-39). Tidzaona AMBUYE posachedwa ili ndi lonjezo. Izi zikuyenera kuchitika nyukiliya ya nkondo yakupha ambiri pakamodzi ndimwankhanza (holocaust) isanafike. Tilibe nthawi yogwiritsa kufikira IYE adzabwera (Chivumbulutso 3:11).

Chizindikiro china cha nthawi yotsiriza MULUNGU ananena kuti mmasiku omaliza IYE adzachita chinthu cha tsopano (Yesaya 43:19). Zaka 2000 zapitazo, Mtumwi Paulo anati, “koma sindidzalola kuti mkazi adzaphunzitse” (1 Timoteo 2:12). Koma Yoweli ndi Mtumwi Petro, mwa MZIMU WOYERA, anati, “Ndipo mtsogolo mwake, ndidzatsanulira MZIMU WANGA pa anthu ONSE [“Onse” kutanthauza kuti aliyense]; ndipo ana anu amuna ndi ana anu akazi adzanenelera [ichi ndichizindikiro chomwe tinali nacho cha chimaliziro, nthawi ya Mtumwi Petro zaka 2000 zapitazo], akuluakulu anu adzalota maloto, anyamata anu adzaona maso mphenya: Ndiponso pa akapolo ndi pa ADZAKAZI omwe mmasiku amenewo [masiku otsilizawa, osati ngati mmasiku a Mtumwi Paulo, zaka 2000 zapitazo. Azibambo ndi azimayi onse patsiku la Pentekositi analandira ubatizo wa MZIMU WOYERA chifukwa anali ataudikilira ndiponso ankaufuna. Ngati ufuna, udzaupenzano,⁷] ndidzakhuthula MZIMU WANGA” (Yoweli 2:28-29, Machitidwe 2:17-18).

5 Luka 9:62, 17:32, Yoh. 15:2, 6, Mac. 14:22, Aro. 11:22, 1 Akor. 15:2, Akol. 1:22-23, 1 Tim. 4:16, 2 Tim. 2:1-3, 12, 4:5, Ahe. 6:4-8, 10:26-31, 35-39, Yak. 5:10-11, 1 Yoh. 2:24-25, 28 6 Dan. 7:7-8, 19-26, 11:31-32, Chiv. 13:1-8, 11-18, chap. 17

Burkina Faso

(Zotanthauziridwa kuchoka mu Chifaransa)

Okonedwa alongo mwa Khristu

Ndiloreni ndikupatseni moni mdzina lopambana ndilotamandika la Ambuye ndi Mpulumutsi Yesu Khristu; limene lili dzina lomwe tinalandilira ulamuliro wopatulika kuti tiyende pamwamba pa mphamvu zonse za mdierekezi mosaopa.

Tikupemphera kuti ambuye adalitse utumiki wanu koposa, ndikukupatsani mphamvu nthawi zonse kuti mupitirize kufalitsa ufumu wa Mulungu. Tinakonda ndithu zosindikizidwa “Kodi ndizolakwika kuti a Khristu obadwanso mwatsopano kuti azigwilira ntchito Boma lopanda umulungu kapena lizigwilira ntchito boma la Mulungu lokha?” Zidutswa zosiyanasiyana za mabuku zimene tinalandira zinatipatsa chilimbikitso. Ndipo monga zilinsotikhudza kukulitsa Ufumu wa Kumwamba, takonza masiku a chitsitsimutso kumene, tidzawerenga zolembedwa zimene talandira kuchokera kwa inu, komanso kugawa kwa iwo amene angathe kuwerenga. Mobwerenza zikomo chifukwa cha zonsezi.

Tikupemphera kuti ambuye Yesu Khristu adalitse utumiki wanu koposa, ndipo ndili ndi chikhulupiliro kuti Khristu akukwenzani m’mwamba m’masiku omalizawa. Chifukwa Iye akutiiza kuti iwo amene sachita manyazi kulankhula za Iye pa dziko lapansili, Iye sadzachita manyazi kulankhula za iwo pamaso pa Atate. Mwalimbikitsa kudziwitsa Khristu pa dziko lonse lapansi, ndipo mphoto yanu idzakhala yapamwamba.

Ndidzakonda kulandiranso zosindikizidwa zanu za chifaransa, ndi ma Baibulo ena kuti tidzapatse anthu osinthika atsopano.

Mulungu wa Mphamvu Zonse akudalitseni!!!

Mafuno athu onse abwino a chaka cha 2012!!!

Bansé Remi

The Evangelism Center of Zoula

Koudougou, Boulkiemdé,

Burkina Faso, Africa

Mneneri Yoweli, kulankhula mwa MZIMU WOYERA, akufunsa anthu nonse pa Yoweli 1:2 zokhudza masiku awa otsiriza: “Imvani izi, akuluakulu inu, nimutchere khutu, inu nonse okhala mdziko. Kodi zinachitikapo n’kale lonse kukhala ndi dziko la boma limodzi chimene chili chinthu chodetsedwa chopangitsa dziko kukhala lotayika?” Kodi munaonapo mwano wotero wa MZIMU WOYERA? Kodi munamvapo za chilorezo choposa chakupha makanda mamiliyoni? Kodi munaonapo chitetezo chobereka chikupatsidwa m’masukulu a boma? Mabanja a pakati pa amuna kapena kapena akazi okhaokha? Kubedwa kwa ana kuchokera kwa makolo achi Khristu? Kodi munaonapo kulowa pansu kotheratu kwa

(Yapitirira patsamba 4)

⁷ Yes. 28:11-12, 44: 3, Yer. 29:12-13, Mat. 3:11, 7:7, Mac. 2:38-39



MAUTUMIKI A ALAMO PA INTANETI

www.alamoministries.com

NDIKOSAVUTA KUNENA NTHAWI YA KUBWERANSO KWA AMBUYE PA DZIKO LAPANSI

(Yachokera patsamba 3)

makhalidwe oyenera ngati mmene ziliri lero? Zamaliseche, zimene zili zopatsa chilakolako cha chiwerewere, kuonetsa chikhumbokhumbo cha kugonana mosaletseka, kulota zoipa, boma lopanda malamulo, ndi zonse zopanda umulungu? Ayi! Palibe!

Inde, MULUNGU adzaononga dziko lapansi komanso oipa ndi moto.⁸ “Koma tsiku la AMBUYE lidzabwera ngati mbala usiku; mmene thambo lidzapita ndi chiphokoso chachikulu, ndipo zam’mwamba zidzakanganuka ndi kutentha kwakukulu, ndipo dziko ndi ntchito zili momwemo zidzathedwa” (2 Petro 3:10). IYE adzafupikitsa nthawi (Mateyu 24:21-22). A Khristu, dikiranibe, YESU adza posachedwa. Inu ofuna kulapa machimo anu kuti mumasulidwe nafe, nenani pemphero ili:

AMBUYE wanga komanso MULUNGU wanga, ndichitireni chifundo ndine munthu wochimwa.⁹ Ndikukhulupirira kuti YESU KHRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.¹⁰ Ndimakhulupiriranso kuti IYE anafera pamtanda ndipo anakhetsa mwazi WAKE wantengo wapatali ndi cholinga choti machimo anga onse akhululukidwe.¹¹ Ndikukhulupiriranso kuti MULUNGU anaukitsa YESU kwa akufa pogwiritsa ntchito mphamvu ya MZIMU WOYERA,¹² ndiponso kuti

IYE anakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo panopa akumva pemphero langa lolapali.¹³ Ndikutsegula zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuyitanani kuti mulowe mumtima mwanga, inu AMBUYE YESU.¹⁴ Tsukani machimo anga ambirimbiri achoke onse mu mwazi wantengo wapatali umene INU munakhetsa m’malo mwanga pamtanda wa ku Kavari.¹⁵ Ndikudziwa kuti mundimvera pemphero langali AMBUYE YESU; INU mukhululukira machimo anga ndi kupulumutsa moyo wanga. Ndikudziwa izi chifukwa MAWU ANU, Baibulo, limanena zimenezi.¹⁶ MAWU ANU amati INUYO simudzakana kumvetsera pemphero la munthu aliyense, ndipo ine ndili m’gulu la anthu amenewo.¹⁷ Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mukundimvetsera pamene ndikupemphera ndipo ndikudziwanso kuti INUYO mundiyankha komanso mundipulumutsa.¹⁸ Ndipo ndikukuthokozani AMBUYE YESU, chifukwa chopulumutsa moyo wanga, ndipo ndisonyeza kuyamikira mwa kuchita zinthu zimene INUYO munalamula komanso kupewa kuchita uchimo.¹⁹

Pambuyo pa chipulumutso, YESU ananena kuti munthu ayenera kubatizidwa pomizidwa thupi lonse m’madzi, m’dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.²⁰ Muziphunzira mwakhama Baibulo la *Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu*, [King James Version] ndipo muzichita zimene Baibulolo limanena.²¹

AMBUYE akufuna kuti inuyo muziwuza ena za chipulumutso chanu. Mungathe kukhala wofalitsa uthenga wabwino wa Mbusa Tony Alamo. Tizikutumizirani mabuku mwaulere. Imbani foni kapena tumizani imelo kwa ife kuti mudziwe zambiri. Tikukupemphani kuti muwuzeko ena uthengawu.

Ngati mukufuna kuti dziko lipulumutsidwe monga m’mene YESU akulamulira, mukufunika kupereka chakhumi kwa MULUNGU. MULUNGU anati, “Kodi munthu angabere MULUNGU? Inde, mwandibera kale. Koma akuti, Ife tikumubera bwanji MULUNGU? Mu chakhumi ndi mu zopereka. Anthuwo ndi otembereredwa chifukwa akundibera, ngakhale mtundu wonsewu [dziko lonse lapansi]. Bweretsani nonse chakhumi [‘chakhumi’ ndi gawo limodzi la magawo khumi (10%) ya malipiro anu] m’nkhoke zanga n’cholinga choti pakhale nyama [chakudya cha Uzimu] mu nyumba YANGA [anthu opulumutsidwa] kuti mundiyese, akutero AMBUYE wa MAKAMU, kuti muone ngati sindidzakutsegulirani mazenera a Kumwamba ndi kukukhuthulirani madalitso amene mudzasowa malo owalandirira.” Ndipo ndidzadzudzula anthu okudyerani masuku pamutu ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhale mphesa wanu sudzalephera kubala zipatso pa nyengo yake m’minda yanu, watero AMBUYE wa MAKAMU. Ndipo mitundu yonse idzakutchani odala: chifukwa dziko lanu lidzakhala labwino, watero AMBUYE wa MAKAMU” (Malaki 3:8-12).

8 Mik. 1:2-4, Mal. 4:1, 2 Ates. 1:7-10, 2 Pet. 3:7-12 9 Sal. 51:5, Aro. 3:10-12, 23 10 Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4 11 Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9 12 Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7 13 Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13 14 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20 15 Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14 16 Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akol. 1:14 17 Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13 18 Aheb. 11:6 19 Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14 20 Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5 21 Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18

Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhani zina zimene zimakusangalatsani, tiimbireni foni kapena tilembere.

Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078

Lamya ya pemphero ndi uthenga maola 24: +1 (661) 252-5686 • Fax +1 (661) 252-4362

www.alamoministries.com • info@alamoministries.com

Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imapereka zinthu zofunika kwa onse amene ali ku U.S. amene akufunitsitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wawo wonse moyo wawo wonse ndi mphamvu zawo zonse

Maservice amachitikira ku New York City lachiwiri lililonse nthawi ya 8 koloko usiku ndi malo ena usiku okhaokha. Chonde imbani +1 (908) 937-5723 kuti mudziwe zambiri. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PAMAPETO PA MAPEMPHERO ALIWONSE.

Funsani buku la M’busa Alamo, lakuti Mesiya, losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.

Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M’busa Alamo

Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n’zaulere, ndipo simulipira ndalama yotumizira

Ngati wina akukuuzani kuti mupereke ndalama pa zinthu zimenezi, chonde imbani pa +1 (661) 252-5686.

M’BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12).

MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENGE.

Anthu amene muli m’mayiko ena, tikukulimbikitsani kuti mumasulire n’chinenero chanu mabukuwa. Ngati mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m’munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:

© Copyright January 2012, 2015 All rights reserved World Pastor Tony Alamo © Registered January 2012, 2015
CHICHEWA/NYANJA—VOLUME 14600—IT IS EASY TO TELL WHEN THE LORD IS COMING BACK TO EARTH